MALAWI-SCOTLAND PARTNERSHIP
MaSP

# SAFEGUARDING POLICY PACKAGE

## CHICHEWA VERSION



MAY 2020

WITH SUPPORT FROM

The Scottish Government
Riaghaltas na h-Alba

Table of Contents

**Malamulo Otetezera Ana ndi Akulu** ........................................................................1

**Malangizo a Bungwe** ........................................................................................................7

**Ndondomeka Zomvera Malipoti ndi Madandu Akuteteza**................................................11

**Lipoti Lofotokozera za Nkhaza**.......................................................................................16

# MALAMULO OTETEZERA ANA NDI AKULU

# Cholinga

Cholinga cha lamuloli ndikuteteza anthu makamaka ana, akuluakulu amene ali pachiwopsezo ndi ena onse amene amapindula ndi ntchito za bungwe la Malawi Scotland Partnership (MaSP). Chiwopsezochi chitha kuchokela kwa amene amagwila ntchito ku MaSP kapena ku ndondomeka yakagwilidwe ka ntchito.

Lamuloli likuwonetsa kudzipeleka kwa bungwe la MaSP ndikulangiza onse ogwila ntchito za udindo wawo pankhani yoteteza anthu.

Lamuloli silikutetezeza iwo amene sagwila ntchito kapena kupindula ndi ntchito za MaSP.

# Kodi kuteteza ndikutani?

Malingana ndi bunge la United Nations, kuteteza kumathandauza kusamala umoyo ndi ufulu wa anthu kuchina chilichonse chimene chingawononge moyo wawo.

Pantchito yathu, kuteteza kumatanthauza kusamala ana ndi akulu kuchiwopsezo chinachilichonse chimene chingawachitikile pakati pa iwo ndi anthu athu ogwila ntchito.

Matanthauzo ena akuteteza alembedwa m'musimu.

# Okhudzidwa

Lamuloli likukhudwa magulu awa:

- Adindo
- Onse olembedwa ntchito ndi bungweli
- Onse ogwila ntchito modzipeleka ndi mwaganyu
- Opelekela katundu, ogwila ntchito mwawukadawulo, alangizi, alendo, atola nkhani, azisudzo ndi andale
- Mabungwe onse amene ali mamembala a MaSP

# Lonjezo Lathu

MaSP ikulonjeza kuteteza ana ndi akulu amene ali pachiwopsezo ndi maufulu a ana mene alili mumalamulo a dziko la Malawi ndi malamulo a nthambi ya bungwe la United Nations (UNCRC). MaSP ikuzindikila udindo wake pakuwonetsetsa kuti maufuluwa akutsatidwa. Bungwe la MaSP lidzaonetsetsa kuti maufulu a ana kapena akulu amene ali pachiwopsezo asaphwanyidwe. Izi zizachitika posatengela kuti munthuyo ndiwa mamuma, wankazi, mtundu, kuthekela kapena chikhalidwe chake.

MaSP inavolemeleza ndi kuzipeleka ku mfundo yokuti 'tisapange nkhaza' ndipo bungweli linayikapo ntima paudindo wake wowonetsetsa kuti antchito ake asazunze, kuchitila chipongwe kapena kuchita zinthu zosayenela.

MaSP ndiyodzipeleka ku udindo wake woteteza anthu kudzela ku ngodya zitatu izi: kupewa, kuwulula ndi kuchitapo kanthu.

# Kupewa

## Udindo wa MaSP

- Idzawonetsetsa kuti onse ogwila ntchito ku bungweli akudziwa za udindo wawo ndi m'mene walembedwela mu malamulowa
- Kukonza ndondomeko ndi kugwila ntchito yake mowonetsetsa kuti anthu onse akutetezedwa kuchiwopsezo chinachilichonse. Izi zikuphatikizapo kapezedwe and kagwilitsidwe ntchito ka mbili ya anthu
- Kukhwimitsa malamulo okhudwa kulemba anthu ntchito, kuyang'anira ogwila ntchito komanso kupeleka ntchito kwa anthu
- Kuwonetsetsa kuti anthu ogwila ntchito akulandila uphungu wankhani yakuteteza malingana ndi udindo wawo m'bungweli
- Kulondoloza madandu onse ndikuchitapo kanthu mwachangu
-

## Udindo wa ogwila ntchito

### Kuteteza ana

Onse ogwila ntchito ku MaSP sayenela kuchita izi:

- M'chitidwe oganana ndi ana osakwana zaka 18
- M'chitidwe ogwirira ana
- Kuchita nkhanza zilizonse kwa ana (monga kumenya, kumumana chakudya, kusamulabadira, kunyoza kapena kumusala)
- Kusagwilitsa ntchito ana pofuna kupeza ndalama kapena kugwilitsa ntchito kapena kugulitsa ana achichepere.
-

### Kuteteza Akulu

Onse ogwila ntchito ku MaSP sayenela kuchita izi:

- Kugwirira kapena kumugona munthu amene ali pachiwopsezo mokakamiza
- Kuchita nkhanza zilizonse kwa anthu amene ali pachiopsezo (monga kumenya, kuwamana chakudya, kusawalabadira, kuwanyoza kapena kuwasala)

### Kuteteza ku nkhaza za m'chitidwe ogonana

Onse ogwila ntchito ku MaSP sayenela kuchita izi:

- Kupeleka thupi lawo kuti apeze ndalama, ntchito kapena zinthu. Izi zikuphatikizaposo chithandizo chimene chimapelekedwa kwa anthu amene amapindula kuntchito za bungwe
- Kuchita m'chitidwe oganana ndi anthu amene amapindula ku ntchito za bungweli chifukwa iwo alibe mphamvu zoti angakane

Mowonjezela, ogwila ntchito ku bungwe la MaSP akuyenelanso kuchita izi:

- Kutengapo mbali pakuwonetsetsa kuti bungweli likupewa ndi kupititsa patsogolo kuteteza kwa maufulu a anthu
- Kuwulula madandu kapena kukayikila kwina kuli konse kumene kungadze pa malo ogwilila ntchito.
-

# KULONGOSOLA MALIPOTI

MaSP idzaonetsetsa kuti njira zopelekera malipoti/madandu ndizoyenela, zotetezedwa ndipo zikupezeka kwa ogwira ntchito ndi m'madera omwe timagwira nawo ntchito.

Ogwira ntchito aliyense amene akupereka madandu kudzerea mnjira zokhazikitsidwa mundondomeko ya bungweli adzatetezedwa ndi malamulo abungweli.

MaSP idzalandira madandu kuchokera kwa anthu amene sitigwila nawo ntchito, mabungwe amene timagwira nawo ntchito komanso maofesi othandizana nawo.

### Njira zoperekera madandu mwachinsinsi

Ogwira ntchito yemwe ali ndi madandu a chinsinsi apereke madandu ake kwa oyang'anira zotetezera anthu pa ntchito (Bambo Mphatso Sapangwa) kapena bwana wake. Ngati munthuyo sali omasuka kupereka madandu kwa anthuwa, mwachitsanzo ngati akuona kuti sathandizidwa moyenerea kapena ngati munthu amudandaulireyo zikumukhudza, akhoza kuperaka madandu ake kwa ogwira ntchito aliyense monga bwana wamkulu kapena kapena kwa aliyense amene ali mu ofesi ya olemba ndi kuchotsa anthu ntchito. Iye akhozanso kupereka madanduwo kwa mkulu wa bungweli pa keyala ili mmusiyi:

The Chief Executive Officer,

Malawi Scotland Partnership,

Area 14, Scripture Union House,

P. O. Box 1589, Lilongwe.

**Email**: info@malawiscotlandpartnership.org

Cell: (+265) 888725600/ 999566648

# Kuyankha Madandu

MaSP idzalondoloza malipoti ndi madandu mogwirizana ndi malamulo a bungweli.

MaSP idzalanga moyenera ogwira ntchito wina aliyense amene waphwanya malmulo a bungweli.

MaSP idzathandiza anthu omwe achitiridwa nkhanza ndi ogwira ntchito kapena othandizira ngakhale ofesi yachitapo kale kanthu (monga kupanga kafukufuku). Ziganizo za m'mene angathandizidwire adzapereka ndi ochitidwa nkhanzayo.

# Chinsinsi

Nkofunika kuti chinsinsi chisungidwe pamene anthu omwe adalandira madandu akufufuza za nkhaniyi. Mfundo zokhudza madandu ziyenera kufotokozeredwa kwa ena pokhapokha zikafunika ndipo payenera kukhala chinsinsi nthawi zonse.

**Zina mwandondomeko zokhudzana ndi malamulowa**

Malamulo a pantchito

Lamulo lothetsa nkhanza

Kuulula m'chitidwe oyipa pa ntchito

Lamulo loteteza ana

Lamulo loteteza akulu

Lamulo loteteza ogwiliridwa ndi ochitidwa nkhanza ndi ogwira ntchito

Lamulo la kaperekedwe ka madandu

Njira zoperekera malipoti ndi mayankho a madandu

Njira zoyenera kutsata polemba anthu ntchito

**Zidzaunikilidwanso pomaliza kwa kafukufuku komanso m'gwirizano ndi MaSP**

Malamulo ena oyenera

# Matanthauzo a Mawu

**Olandila Chithandizo**

Amene akulandira katundu ndi chithandizo china chilichonse kuchokera ku bungwe la MaSP. Dziwani kuti kugwiritsa ntchito mphanvu molakwika kungathe kukhudza madera ena omwe bungweli limagwirako ntchito komanso kukhoza kubweretsa nkhanza powapatsa anthu chithunzithunzi kuti inu muli ndi mphamvu.

**Mwana**

Mogwirizana ndi malamulo a dzilo la Malawi, munthu yemwe sadakwanitse zaka 18 ndi mwana (Malamulo okhudza ufulu wa ana).

**Nkhanza**

Kumuphwanyira munthu ufulu wachibadwidwe komanso kumuchitira nkhanza. Nkhanzazo zingathe kukhala za m'malingaliro kapena zapathupi.

**Nkhanza za m'malingaliro**

Nkhanza za m'malingaliro ndi monga kunyazitsa potchula mayina oyipa, kunyoza kopitiriza, kuchepsa ndi kumpatula.

**Kuteteza Kumchitidwe ogwilira ndi nkhanza**

Izi zimatanthauza kupewa m'chitidwe ogwilira ndi nkhanza kwa anthu kuchokera kwa ogwira ntchito.

Mauwa anatengedwa m'kabuku kolembedwa ndi mlembi Wamkulu wa United Nations (ST/SGB/2003/13)

**Kuteteza**

Ku UK kuteteza kumakhudza umoyo wa anthu, ufulu wachibadwidwe, komanso kuwonetsetsa kuti anthu akukhala momasuka, mopanda nkhanza ndi chiopsezo chinalichonse.

M'bungwe lanthu kuteteza kumatanthauza kuti anthu, kuphatikizapo ana ndi akuluakulu omwe ali pachiopsezo ku nkhanza zimene zingabwere chifukwa chokumana ndi ogwira ntchito athu kapena mapologaramu athu akhale otetezedwa.

Mmodzi amene amathandiza bungweli anapereka tankhauzo ili:

Kuika ndondomeko zopewera nkhanza makamaka m'chitidwe ogwilira kuti zisachitike; kuteteza anthu makamaka akulu ndi ana amene ali pachiopsezo kunkhanza; komanso kutengapo gawo mwachangu pamene nkhanza yachitika. Tanthauzoli limaonetsetsa za kuteteza komanso kutengapo gawo ku nkhanza yomwe ingachitike, yachitika, kapena pamene pali kugwiritsa ntchito mphamvu molakwika, kukhulupilika, kapena chiopsezo makamaka chokhudza m'chitidwe ogwilira.

Kuteteza kumapezeka mmagawo amapologaramu athu onse, ogwira nawo ntchito ndi ogwira ntchito. Zimafunika kuti apeze, ateteze zoopsa za nkhanza, kukhala ndi ndondomeko zodalilika, kutenga gawo ndi kupereka lipoti ndi kuphunzira pamene pali chiopsezo. Ndondomeko zimenezi zimayenela kukomela iwo amene achitiridwa nkhanza komanso kuteteza amene akuganiziridwa mpaka atapezeka kuti ndiwolakwa.

Kuteteza kumaika anthu opindula komanso okhudzidwa pakati pazonse zomwe timapanga.

**Nkhanza zogonana**

Izi zimatanthauza kuchita m'chitidwe ogonana ndi munthu momukakamiza kapena kumunyengerera.

**Kupindula ndi m'chitidwe ogonana mokakamiza**

Kugwilitsa ntchito mphamvu molakwika kuti ugonane ndi munthu kuphatikizapo kumugwilitsa ntchito kuti upindule munjira zosiyanasiyana. Tanthauzoli likuphatikizapo m'chitidwe ozembetsa anthu komanso ukapolo wamakono.

**Wochitidwa Nkhanza**

Uyu ndi munthu amene wachitidwa nkhanza. Mauwa amatanthauza kuti munthuyu anachitidwa chipongwe ndipo anapulumuka, anawonetsa kupilira, kulimbika, kuthekera, ndi chikhumbokhumbo chofuna kukhala ndi moyo. Ngakhale izi zili chomwechi munthuyu ali ndi ufulu osankha dzina limene azitchulidwa nalo.

**Akulu amene ali pachiopsezo**

Munthu amene akufunika chisamaliro chifukwa cha mavuto a ubongo kapena ulumali wina uliwonse, ukalamba kapena matenda; kapenanso amene akulephera kudziteteza yekha ku nkhanza zosiyanasiyana.

# MALANGIZO A BUNGWE

## Chiyambi

Polimbikitsa zolinga za mgwilizano pakati pa Malawi ndi Scotland komaso pakati pa a Malawi onse pafunika ku khala mgwilizano weni weni pakati pa boma la Malawi komaso la Scotland kuti tisunge chikhalidwe pakati pogwila ntchito ndi ena onse okhudzidwa. Polimbikitsa gwilizanowo, zolinga za MaSP ndi ogwila awo komaso onse othandizila ntchitozi.

## Zolinga

Malangizowa akukhudza anthu ogwila ntchito, aganyu, ogwila ntchito mozipeleka ndi opelekela a katundu osiyana siyana ku bungwe la MaSP

Cholinga cha malangizowa ndicho kukwanilitsa zomwe MaSP imayembekezela kwa ogwila ntchito ake polingana ndi mgwilizano wawo wakagwilidwe ka ntchito; ndipo izi ziyenela kutsatidwa nthawi zonse. Osatsatila malangizowa aza landila chilango kapena kuchotsedwa ntchito

MaSP ndi bungwe la aMalawi ndipo limatsogozedwaso ndi aMalawi. Malangizowa anakonzedwa mowunikilidwa ndi malangizo ena okonzedwa ndi ma bungwe akulu akuku a dziko la pansi monga United Nations. Ogwila ntchito ku bungwe la MaSP ayenela kutsata malamulo a dziko lawo mosamalitsa zolinga za MaSP.

## Nsanamila za Bungwe la MaSP

Bungwe la MaSP ndima membala ake amatsatila nsanamila izi: kukonza madongosolo antchito ndi kugwilila limodzi, osasiya munthu mbuyo, osapangila munthu nkhanza, kupanga zoyenela, kulemekezana, kukhulupilirana ndi kumvetsetsana, kugwila ntchito moyenela, kugwila ntchito molumikizana, kugwila ntchito mopanda chinyengo, mothandizana ndi mowona patsogolo.

# Malonjezano a Malangizo

Ine ngatim'dindo, olembedwa ntchito, odzipeleka, othandizila ndi mlendo ndiku lonjeza kuti:

**Ndizalemekeza ndi kuteteza mbili ya bungwe la MaSP pochita izi**

- Polemekeza anthu onse
- Posamala malamulo amaiko ena ndi kusamala chikhalidwe cha anthu akumeneko.
- Powonetsetsa kuti zochita zanga sizikubweletsa manyazi ku bungwe la MaSP
- Posaledzela kapena kugwilitsa ntchito mankhwala ozunguza bongo pamene ndili pamalo antchito

**posatenga nawo mbali pozunza kapena kuchitila nkhanza anthu ena**

- Posachita mchitidwe ogonana ndi ana ochepela zaka 18 zakubadwa. Kusadziwa zaka za mwana sichifukwa chokwanila.
- posazagulitsa thupi langa kapena kuchita mchitidwe uliwonse kuti ndipeze ntchito. Izi zikukhudzanso anthu amene amapindula ntchito zathu.

- Posachita chibwenzi ndi anthu amene amapindula ndi ntchito zathu
- Posalemba ntchito ana kapena ena ovutika ndi anthu ena ali pachiwopsezo komaso kuwagulitsa mowazembetsa kuti ndipeze ndalama mosavuta
- Posamenya ana kapena anthu ena apachiwopsezo
- Posazunza m'maganizo ana kapena anthu ena apachiwopsezo
- Posapeleka thupi langa ndikuzinyazitsa kuti ndipeze ndalama, ntchito, katundu kapena kukonderedwa kulikonse. Izi zikukhuzanso onse amene amathandizidwa ndi bungwe lathu

**Kuwonetsetsa chitetezo, thanzi ndi umoyo wa anthu ogwila ntchito ku bungwe la MaSP**

- Potsatila malamulo onse za chitetezo ndi za umoyo pamalo antchito
- Potsatila ndondomeko zachitetezo zamudela lathu ndikudziwitsa mabwana zakusintha kuli konse
- Powonetsetsa kuti khalidwe langa pamalo antchito likuteteza ine mwini komanso anthu onse ogwila nawo ntchito angakhale amabungwe ena

**Kuwonetsetsa kuti zida zonse zogwilila ntchito zimene zili m'manja mwanga ndizotetezedwa:**

- Powonetsetsa kuti ndikusamala moyenela zida zonse zogwilila ntchito kuphatikizapo ndalama
- Posagwilitsa ntchito makina a intaneti mowononga komaso mosatsatila malamulo a dziko kapena a dziko lonse lapansi zimene zimapangitsa kupalamula mulandu. Izi zikuphatikiza mfundo zonse zimene zinyazitsa kapena kuwopseza magulu ena kapena zothandizila m'chitidwe wa upandu.
- Posagwilitsa ntchito makina a intaneti a bungwe la MaSP kuwonela, kusunga, ngakhale kugawa zinthu zotukwana, zolawula, zonyoza, ngakhale zowonetsa m'chitidwe ozunza ana achichepele.

**Magwilidwe anga antchito asatsutsane ndi moyo wanga wa tsiku ndi tsiku:**

- Ponena poyela ngati pali ubale pakati pa ine ndi anthu amene akugulitsa katundu, kapena ukadawulo ku bungwe la MaSP
- Podzipatula pazokambilana zimene zingapereke ntchito, kukweza udindo kwa munthu amene ndili naye pam'gwilizano wa nkhani za chuma, za chikondi kapena m'bale wanga
- Popempha chilolezo ndisanavomele kutenga nawo gawo pa nkhani za ndale.
- Posalandila mphatso kuchokela kwa anthu ogwila ntchito m'boma, akumadela kumene timagwila nawo ntchito, akumabungwe ena, opelekela katundu ndi ukadawulo

**Kusunga chinsisi**

- Posamalitsa zinsisi zonse za ntchito ndi posawulula nkhani zokhudza anthu ogwila ntchito ku bungweli; pokhapokha nditafunsidwa kuchita izi ndi lamulo.

# Ndondomeko ya Madandu

Onse ogwila ntchito ku bungweli akuyenela kuwonetsetsa kuti afotokoza kwa mabwana awo zimene awona, awuzidwa komanso zimene akuganizila kuti zachitika motsutsana ndi malangizowa. Zonse zimene zizanenedwe zizasungidwa mwa chinsisi molingana ndi malamulo a ntchito (Disclosure of Malpractice in the Workplace policy)

Ogwila ntchito onse amene ali ndi madandu akafotokoze kwa mabwana awo. Kwa iwo amene saali omasuka kutelo akhoza kufotokozela nzawo kuofesi kapena wina aliyense amene amagwila ntchito yolemba ndi kuchotsa anthu ntchito m'bungwelo (HR department)

Ogwila ntchito onse amene alandila madandu akuyenela kuchitapo kanthu mwachangu kapena kupeleka uthengawo molingana ndi malamulo a kayendetsedwe ka madandu a bungweli.

# Malangizo Ogwilizana Nawo

Malangizo otetezela anthu

Malangizo otetezela ana

Ndondomeko ya madandu

---

Povomela ntchito ndikulonjeza kudzagwila motsatila malamulowa.

**Dzina:**

**Sayini:**

**Tsiku:**

# NDONDOMEKO ZOMVERA MALIPOTI NDI MADANDU AKUTETEZA

# Cholinga

Cholinga cha zolembedwazi ndicho kupereka ndondomeko ya zinthu zoti zichitidwe pamene malamulo otetezela aphwanyidwa motere:

- Kwa ogwira ntchito kapena munthu wina ali yense
- Pamene malamulowa aphwanyidwa ndi ogwira ntchito athu, anthu ogwira ntchito ku mabungwe ena kapena anthu omwe amagwira nafe ntchito.

# Ndondomeko

**1. Kulandira malipoti**

1.1 Malipoti akhoza kufika ku bungweli kudzera njira zosiyanasiyana. Munthu akhoza kupita payekha, kulemba kalata, kutumiza mauthenga a pafoni, kapena mauthenga osiyasiyana odzera makina a intaneti. Maunthengawa atha kuchokelanso kumphekesera. Ngati ogwira ntchito wamva mphekesera ndipo waganizira kuti zikukhudza madandu, akuyenera kufotokozera amene amalandira madandu m'bungweli.

1.2 Pamene madandu aperekedwa kwa ogwira ntchito, wolandirayo akuyenera kuganizira izi:

- Kumvetsera
- Kugawana malingaliro ndi wodandaulayo
- Kufunsa mafunso monga; ndani, liti, kuti koma osati chifukwa
- Kubwereza kufotokozera pofuna kuonetsetsa kuti mwamvetsa momwe zinthu ziliri
- Kufotokozera kwa amene amalandira madandu

1.3 Munthu wolandira madandu ayenera kulemba zotsatirazo kugwiritsa ntchito fomu:

- Dzina la munthu amene akupereka madandu
- Maina a amene akuganiziridwa kuti achitiridwa nkhanza ngati asiyana ndi am'mwambawa
- Maina a amene akuganiziridwa kuti achita nkhanza
- Kufotokozera za zimene zidachitika
- Masiku, nthawi ndi malo amene zinthuzo zidachitikira

1.4 Munthu amene akulandira malipotiyu akuyenera kutumiza kwa munthu amene amalandira madandu azotetezela pasanathe tsiku limodzi.

1.5 Chifukwa cha kuopsa kwa nkhaniyi, chinsinsi chikuyenera kusungidwa mmagawo onse amene amatsatidwa popereka malipoti, komanso mfundo zimene zimagawidwa pokhapokha zikafunika. Izi zikukhudzanso mabwana akuluakulu pa ofesi.

1.6 Pamene ogwira ntchito amene wapereka madandu sadakhutitsidwe ndi m'mene bungweli likuyendetsera madandu ake, ali ndi ufulu wokapereka madandu kumaofesi ena pabungwe pomwepo kapena mabungwe ena akunja. Ogwira ntchitoyo adzatetezedwa ku zotsatira zoipa zimene zingabwere chifukwa choti wapereka nkhaniyo ku maofesi ena. Kuti mudziwe zambili onani malamulo okhudza madandu ndikuulula zakachitidwe ka nkhanza pamalo ogwira ntchito.

**2. Kuunika kapitilizidwe kamalipoti**

2.1 Kusannkha wopanga chiganizo pamene nkhaniyo ikuunikidwa.

2.2 Kuunika ngati nkhaniyo ikuyenera kupitilira

- Kodi lipoti limene lalandiridwalo likusonyeza kuphwanya lamulo loteteza?
- Kodi pali umboni wokwanira kuti lipoti lifufuzidwe?

2.3 Ngati lipoti lomwe lalandiridwa silikusonyeza kuphwanya malamulo a bungwe koma likupereka chiopsezo kwa anthu ena likuyenera kutumizidwa kwa atsogoleri a m'madera ngati ndikoyenera kutero.

2.4 Ngati palibe umboni wokwanira pa lipoti limene lalandiridwa, mwachitsanzo ngati munthu wopereka lipotiyo sadasiye dzina ndi kumene akuchokera, lipotili likuyenera kusungidwa kuti lizagwile ntchito m'tsogolo.

2.5 Ngati lipotilo kukukhudza ana omwe sadakwane zaka 18, funsani upangiri kuchokera kwa anthu amene amaona nkhani za ana nthawi yomweyo. Ngakhale pamene kafukufuku wa nkhani akupangidwa aliyense amene akukhudzidwa munkhani ngati sadakwane zaka 18, opanga chiganizo akuyenera kuuzidwa komanso ayenera kupeza upangiri kwa anthu amene amaona nkhani zokhudwa ana.

2.6 Ngati pali chiganizo kuti nkhaniyo ipitilire, oona nkhaniyo akuyenera kukhala ndi ukadaulo woyenerera wokhudza nkhaniyo. Ngati kulibe upangiri m'bungwelo, ayenera kupempha kuchokera kwa ena ngati kuli koyenera kutero.

2.7 Muonetsetse kuti ndi zinthu ziti mulipotilo zimene mungagawane ndi ena komanso motani. Onetsetsani kuti chinsinsi chasungidwa nthawi zonse, ndipo nkhaniyi ikuwuzidwa kwa iwo okha akuyenela kudziwa. Pangani ziganizo pa mfundo zimene mungagawane ndi anthu ena; chifukwa zofuna za wanthu zimasiyana.

2.8 Pakhoza kukhala malamulo osiyanasiyana ndi mmene nkhaniyo ilili. Mwachitsanzo m'chitidwe wankhani zogonana pamalo a ntchito umaunikidwa ndi malamulo okhudzana ndi nkhani ya chitonzo ndi kuzunzana.

Ngati palibe lamulo logwirizanan ndi lipoti limene mwalandira muyenera kutsatira ndondomeko zatchulidwazi.

2.9 Muonetsetse kuti mwafotokozera mabungwe onse oyenerera pamene mwalandira lipoti.

Mabungwe ndi monga:

- Omwe amakuthandizani pa chuma
- Mabungwe akuluakulu omwe muli pansi pawo
- Malamulo ndi ndondomeko za m'gwilizano

Ena mwa mabungwewa adzafuna kuti muwafotokozere pamene mwalandira lipoti, ena adzafuna lipoti ya mmene mlandu wayendera kapena mmene milandu yayendera chaka chonse. Mukamapereka malipotiwa kwa mabungwe amenewa, muyenera kuganizira mozama za chinsinsi.

**3. Sankhani Maudinto ndi Zochitika za Milandu**

3.1 Ngati maudindo sanasankhidwe musankhe wopanga chiganiza pamlandu. Iye ayenera kukhala ogwira ntchito amene ali ndi udindo waukulu komanso amene sakukhudzidwa ndi mlanduwo munjira ina iliyonse.

3.2 ngati lipoti likuwonetsa kuphwanya kwa malamulo akuteteza, mungathe kupanga mkumano umene ungakhale ndi anthu otsatirawa:

- Wopanga chiganizo
- Munthu amene analandira lipoti
- Wolemba anthu ntchito
- Mlangizi pa nkhani zoteteza anthu ngati alipo (kapena ofanana naye paudindowu)

Nkumanowu ukuyenera kupeza njira zimene zingatetezere kapena kupereka chithandizo kwa anthu amene achitidwa nkhanza ndi ena onse okhudzidwa.

**4. Kupereka chithandizo kwa ochitidwa nkhanza ngati kuli kofunika**

4.1 Kupereka chithandizo choyenera kwa amene achitilidwa nkhanza. Izi ziyenera kukhala choncho ngakhale lipolito silinafufuzidwe. Chithandizo chikuyenera kukhala motere:

- Kulandira uphungu
- Kulandira chithandizo cha kuchipatala
- Kulandira chitetezo, mwachitsanzo kupititsidwa kumalo otetezeka

4.2 Chisankho cha mmene chithandizo chingakhalire chikuyenera kutsogozedwa ndi amene wachitilidwa nkhanza.

**5. Kuunikira chitetezo kapena chiopsezo cha amene mumagwira nawo ntchito**

5.1 Kwa malipoti amene nkhani zake ndi zoopsa: akuyenera kufufuza chiopsezo mmene chilili kwa anthu amene mumagwira nawo ntchito wokhudza mlanduwu nkupeza njira zochepetsera chiopsezocho ngati kuli koyenera.

5.2 Kupitiriza kuonanso chiopsezo mmene chilili ndi kupezanso njira pafupipafupi pamene mlanduwo ukuyendetsedwa kapena watha.

**6. Kuona njira zina**

6.1 Wopanga chiganizo amaonanso njira zina. Izi zikhoza kukhala

- Kuthetsa nkhaniyo panjira (ngati palibe umboni wokwanira kapena ngani nkhaniyo siikukhudza bungwelo)
- Kafukufuku ayenera kuchitidwa kuti mupeze mfundo zokwanira
- Kupereka chilango mwachangu ngati sipakufunikanso umboni wina
- Kupereka nkhaniyo kwa adindo ena

6.2 Ngati lipoti ikukhudza anthu ena omwe amathandizila bungweli (monga azomangamanga, opereka upangiri ndi ogulitsa katundu), njira yopangira chiganizo idzakhala yosiyana. Ngakhale anthu amenewa siogwira ntchito kubungweli tili ndi udindo owateteza. Sitingatsatire zilango zimene zima perekedwa kwa anthu ogwila nage ntchito kwa anthu omwe sagwila ntchito ku bungweli, komabe ziganizo zina zikhoza kupangidwa monga kuyimitsa m’gwilizano wogula katundu chifukwa chakhalidwe la anthu awo ogwila ntchito.

6.3 Ngati kafukufuku akufunika ndipo bungweli lilibe kuthekera, akhoza kupeza ena amene angapange kafukufukuyo. Apangenso chiganizo za komwe ndalama zopangira izi zingachokere.

## 7. Kuyendetsa kafukufuku ngati kuli koyenera

7.1 Onani ndondomeko zofufuzira kuphwanya malamulo, ngati njira zopangira kafukufuku sizikukwanira, mungathe kugwiritsa ntchito malamulo ena omwe asali abungweli.

## 8. Kupanga chiganizo pazotsatira za lipoti ya kafukufuku

8.1 Wopanga chiganizoyo amapereka mfundo mogwirizana ndi lipoti la kafukufuku. Ziganizo zogwirizana ndi madandu ziyenera kupangidwa mogwirizana ndi malamulo komanso ndondomeko za kuphwanya malamulo kwa ogwira ntchito.

8.2 Ngati pali kuganizilidwa kwa m'chitidwe wa upandu pamene mlandu uli mkati, mlanduwu ukhoza kupititsidwa kwa oyenera pokhapokha ngati okhuzidwayo ali pachiopsezo. Zikatero opanga chiganizo ndi adindo ena adzafunika kuona kuti nkhaniyo aipitiriza motani. Chiganizochi chikuyenera kupangidwa poganizira chiopsezo chimene chingabwere kwa onse okhudzidwa, ochitilidwa nkhanza ndi oganiziridwa.

## 9. Kutseka mlandu

9.1 Ziganizo zonse za mlanduwu zilembedwe bwino komanso mwachinsinsi.

9.2 Sungani mfundo zonse zokhudza mlanduwu mwachinsinsi mogwirizana ndi malamulo abungwe lathu.

9.3 Lembani mfundo zonse zachinsinsi zokhudza mlanduwu kuti zidzagwiritsidwe ntchito pomadzachita malipoti komanso kuthandizira kuphunzira m'tsogolo (monga ngati malipoti opita kwa adindo, kapena othandizira bungweli pazachuma).

# LIPOTI LOFOTOKOZERA NKHAZA

Fomu iyi iyenera kugwiritsidwa ntchito polemba nkhanza zimene zachitika zokhudza ana kapena anthu ena omwe ali pachiopsezo. Ngati zachititika mwadzidzidzi, chonde musachedwe kudwizitsa a polisi kapena mabungwe ena amene amagwira ntchito ngati zimenezi. Mfundo zonse ziyenera kusungidwa mwachinsinsi ndi kuperekedwa kwa oyenera lisanatha tsiku limodzi kapena tsiku lina logwira ntchito ngati zachitika kumapeto kwa sabata.
Fomuyi iyenera kulembeswa panthawi yomwe mwauzidwa za m'chitidwe wa nkhanza koma mutatsatira ndondomeko zonse zomwe ziyenera kutsatidwa. Chonde lembani fomu yonseyi mwatsatanetsatane.

| **1. Mbiri yokhudza munthu wolemba fomu** | |
|---|---|
| Dzina | |
| Udindo | |
| Telefoni | Email |

| **2. Mbiri yokhudza munthu wokhudzidwa** | |
|---|---|
| Dzina | |
| Udindo | |
| Telefoni | Email |

| **3. Tsatanetsatane wa zimene zidachitika (chonde fotokozani tsatanetsatane pogwiritsa ntchito mfundo zokha)** |
|---|
| Tsiku________________Nthawi<br>____________Malo______________________ |
| |

| **4. Mbiri za mboni/ amene analipo panthawi ya zochitikazo** | |
|---|---|
| Dzina | |
| Keyala | |
| Telefoni | Email |
| Dzina | |
| Keyala | |
| Telefoni | Email |

| **5. Mfundo zina zoonjezera zimene mukuona ngati ndizofunika kwambiri** |
|---|
| |

Ndalemba fomuyi ndikupereka mfundo zomwe ndi zoona, ndipo izi, simaganizo anga.

Dzina……………………………………………………Sayini…………………………Tsiku…………………….






For further details please contact:
The Chief Executive Officer
Malawi Scotland Partnership
Area 14 plot number 14/008
Scripture Union House (Opposite CCBC)
P.O Box 1589
Lilongwe, Malawi

info@malawiscotlandpartnership.org
www.malawiscotlandpartnership.org

Malawi Scotland Partnership
Malawi Scotland Partnership